Parables of Jesus/Women of the Bible (Chinyanja)
First Published by the Baptist Publishing House
Box 1995, Lusaka, Zambia

7008

# MAFANIZO A YESU





# AZIMAI AM'BUKU LOPATULIKA

Mary Small


Parables of Jesus/Women of the Bible (Chinyanja)
First Published by the Baptist Publishing House
Box 1995, Lusaka, Zambia

7008

# MAFANIZO A YESU



# AZIMAI AM'BUKU LOPATULIKA



Mary Small

W234
NYA

PARABLES OF JESUS/WOMEN OF THE BIBLE
(Chinyanja)

First Published
1 Oct. 1979

By the
Baptist Publishing House
P. O. Box 1995
Lusaka, Zambia

adzatipatsa nzeru zotithandiza pa mabvuto athu. Iye adzatipatsa mtendere m'mitima yathu, ngakhale pamene mabvuto adzatizungulira.

MTSOGOLERI:

Tiyeni tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize ife kuti tikhale ndi nthawi ndi iye tsiku ndi tsiku. Muthokozeni cifukwa ca maphunziro amene takhala tiri kuphunzira masabata apitawa.

PEMPHERO:



MAFANIZO A YESU


| MUTU | | TSAMBA |
|---|---|---|
| 1. | Nkhosa Yosocera | 1 |
| 2. | Wofesa | 3 |
| 3. | Matalente | 6 |
| 4. | Mkazi Wamasiye, Ndi Woweruza Wosalungama | 10 |
| 5. | Munda wa Mphesa ndi Olima Munda | 13 |
| 6. | Mwini Cuma Wopusa | 16 |
| 7. | Anamwali Khumi | 20 |
| | AZIMAI AM'BUKU LOPATULIKA | |
| 8. | Rute | 24 |
| 9. | Estere | 28 |
| 10. | Mariya, Mai wa Yesu | 33 |
| 11. | Mariya ndi Marita | 38 |

Posacedwa Mariya, anaturuka kudzakomana ndi Yesu. Iyenso anafotokoza mau amodzi modzi omwe Marita ananena. Yesu anaona kusakondwa kwa abwenzi ace. Iyenso anali wosakondwa. Ndipo analira. Ndipo Yesu anapita ku manda a Lazaro. Musaiwale kuti Lazaro nthawi imeneyi anali atafa masiku anai. Yesu analamulira kuti acotse mwala pakhomo la manda ndipo anati, "Lazaro, turuka" (Yoane 11:43b).

Ndiri kuganiza kuti Mariya ndi Marita anali wodabwa pamene anaona kuti mbale wao ali ndi moyonso. Mwina iwo sanaganizire kuti Yesu adakakhoza kuutsa Lazaro kwa akufa pa nthawi imeneyi. Ndipo iwo anali wokondwa.

GAWO LACINAI:

Tsopano tiyeni tiganizire za zinthu zina zomwe tingaziphunzire kucokera kwa Mariya ndi Marita. Poyamba ganizirani za funso iri. "Kodi inu mumakhala nthawi yaitali yotani tsiku ndi tsiku ndi Yesu?"

Mwina mwace muli kuganizira kuti, "Eya, ngati Yesu akadakhala m'mudzi mwathu masiku ano monga anali kukhalira ku Betaniya kale, ndikadakhala pa mapazi ace ndi kumamvera ziphunzitso zace." Kodi inu mukadakhala monga Mariya, kumvetsera kwa Yesu? Kapena mukadakhala monga Marita, wokhala wotanganidwa nthawi zonse kukonza cakudya ndi kutumikira? Ndi cinthu capafupi kuyankha, kuti, "Ndikadakhala monga Mariya."

Kodi tsopano ziri zotani m'moyo wanu? Mau apamtima athu ndi mau a Yesu: "Muli abwenzi anga inu, ngati muzicita zimene ndikulamulirani inu" (Yohane 15:14). Nthawi zonse timayenera kutenga nthawi yophunzira za Mulungu. Pamene ife tiri kuwerenga Buku Lopatulika, Mulungu amalankhula kwa ife. Pamene ife tiri kupemphera, timalankhulana ndi Mulungu. Ndi cinthu cabwino nthawi zonse kumakhala ndi kamphindi komawerenga mau a Mulungu ndi kumapemphera.

Pamene ife tiika Yesu m'moyo wathu kukhala oyamba, monga Mariya, Mulungu adzatipatsa mphamvu yogwirira nchito yathu. Iye

anandisiya nditumikire ndekha? Mumuuze tsono kuti andithandize" (Luka 10:40b).

Kodi Yesu anapereka yankho lotani? (Werengani Luka 10:41-42.) Marita anakonda Yesu. Anakhulupirira mwa Iye. Ndipo anafuna kumukonzera zinthu. Komabe sanatenge nthawi yofuna kumvetsera ziphunzitso zace ndikuti aphunzire zinthu za Mulungu. Yesu anamuuza kuti ali kusowekera kanthu kena. Iyenso anafunika kusankha comwe Mariya anacisankha.

Yesu anadziwa kuti iye sadzakhala padziko lapansi kwa nthawi yaitali. Yesu anadziwa zoonadi zomwe Mariya ndi ena anaziphunzira kuti zizakhala nawo akadzacoka ndi kupita kumwamba.

GAWO LACITATU:

Tsopano tiyeni tiganizire za nthawi ina ya moyo wa banja limeneli. Pezani Yohane mutu 11 mu Buku Lopatulika lanu.

Lazaro, mbale wa Mariya ndi Marita anali kudwala. Yesu anali kwina kutali ndi Betaniya. Komabe Marita ndi Mariya anatumiza mthenga kwa Yesu za Lazaro. Buku Lopatulika limatiuza kuti, "Cifukwa cace pamene anamva kuti anadwala (Lazaro) (Yesu) anakhala pamenepo pa malo pomwepo masiku awiri" (Yohane 11:6). Ndipo Yesu analamulira kuti apite ku Betaniya.

Poyamba akuphunzira anaganizira kuti Lazaro anali kudwalabe. Koma Yesu posiriza ananena kuti, "Lazaro wamwalira. Ndipo ndikondwera cifukwa ca inu kuti kunalibe Ine komweko, cakuti mukakhulupire koma tiyeni, tipite kwa iye" (Yohane 11:14b-15).

Pamene Marita anamva kuti Yesu ali kubwera, iye anaturuka ndikukamucingamira. Iye anati kwa Yesu, "Ambuye, mudakakhala kuno mlongo wanga sakadafa" (Yohane 11:21). Yesu anamuuza iye kuti mlongo wako adzaukanso. Iye anabvomereza kuti adzaukanso pa nthawi ya cimaliziro. Koma cimeneci sicimene Yesu anali kulankhula.



MUTU 1

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU
PHUNZIRO LALERO: NKHOSA YOSOCERA
MAU A MULUNGU: Luka 15:1-7

MAU APAMTIMA: "Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse."
Yesaya 53:6

MTSOGOLERI:

Lero tidzayamba kuphunzira ena a mafanizo a Yesu. Kodi fanizo ndi ciani? Fanizo ndi nthano yokhudza cinthu cina padziko lapansi pofuna kuphunzitsa zoonadi za Mulungu. Ndi cithunzithunzi cofuna kutithandiza ife kuti timvetse bwino zoonadi za Mulungu. Limaphunzitsa coonadi cimeneci m'njira yapafupi ndithu. Nthawi zambiri Yesu anali kugwiritsa nchito mafanizo pophunzitsa zinthu za Mulungu. Anali kulankhula za zinthu zimene anthu anali kudziwa bwino. Anali kulankhula za mbeu ndi wofesa mbeu. Anali kulankhula za mbusa ndi nkhosa yotaika. Analankhula za wacuma cambiri koma mlimi wopusa; Tidzaphunzira za mafanizo amenewa ndi enanso m'masabata alikubwelawa.

GAWO LOYAMBA:

Phunziro lalero ndi la nkhosa yosocera. Tsiku lina anthu ambiri anabwera kudzamvetsera mau a Yesu. Ambiri a anthuwa anali a m'sonkho ndi ocimwa. M'nthawi ya Yesu anthu a misonkho anali kuzondedwa ndi anzao; Anali kuzondedwa cifukwa nthawi zambiri anali kubela anthu powasonkhetsa msonkho wambiri. Anali kucita izi kuti naonso akhale ndi cuma. Afalisi ndi Alembi anali atsogoleri a cipembedzo. Anayamba kudandaula. Anati "Munthu uyu alandira anthu ocimwa nadya nao" (Luka 15:2). Kwa iwo cotereci Yesu sakanayenera kucicita. Koma Yesu akonda anthu onse. Anawakonda, amsonkhowo, pamodzi ndi ocimwawo.

GAWO LACIWIRI:

Pofuna kuti athandize afalisi ndi Alembi kuti amvetse cifukwa cimene Yesu anali kukhalira pamodzi ndi anthu ocimwa Yesu anauza anthuwo kanthano. Anayamba kulankhula za munthu amene anali ndi nkhosa makhumi khumi imodzi ya nkhosazo inasowa. Yesu anafunsa funso, "kodi munthu acita ciani?" Ndi zoona kuti azasiya zina zonse nayamba kufuna funa yosowayo. Anafunafuna kufikira atapeza yosowa.

Ataipeza, amaitenga kunyumba. Amakhala wokondwa kwambiri cifukwa apeza nkhosa yosowa. Inu pamene mutaya kanthu kena, mumacita ciyani? Kodi mumakondwera mutakapeza?

GAWO LACITATU:

Tsono Yesu analankhula mau okondweletsa kwambiri. Anati "Ndinena kwa Inu, kotero kudzakhala cimwemwe kumwamba cifukwa ca wocimwa mmodzi wotembenuka mtima, koposa anthu olungama asanu ndi anai, amene alibe kusowa kutembenuka mtima" (Luka 15:7).

GAWO LACINAI:

Mu Yesaya 53:6 timawerenga mauwa: "Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse."

Anthu amene amadziwa za nkhosa ndi kudzisunga amatiuza kuti sidzikhoza kudzithandiza zokha angakhale pang'ono. Nkhosa zimasamira pa mbusa kuti adzisogolere ku cakudya cabwino, madzi abwino ndi kudzisunga. Ngati imodzi isocera, siikhoza kubwelera kumene kuli zinzace. Mbusa ayenera kukaifunafuna.

Ndime imene tawerenga kucokera m'buku la Yesaya itiuza ife kuti tiri monga nkhosa. Tasocera. Timafunika mbusa wabwino kuti atitsogolere. Mulungu anatipangira njira yakuti ife tingapulu-



ena anadandaula za cimeneci. Koma Yesu anati, "Mleke iye, pakuti anacisungira ici tsiku la kuikidwa kwanga" (Yohane 12:7). Mu Mateyu ndi mu Marko Yesu anati, "Indetu ndinena kwa inu, kumene kuli konse uthenga uwu wabwino udzalalikidwa m'dziko lonse lapansi ici cimene mkaziyo anacitaci cidzakambidwanso cikumbukiro cace" (Mateyu 26:13 ndi Marko 14:9). Ndipo tsopano ngakhale lero ciri kunendwa pokumbukira za Mariya.

Koma tiyeni tibwererenso kuti tiphunzire za banja limeneli ndikuti ndicifukwa ciani anali abwenzi abwino a Yesu. Mariya, Marita ndi Lazaro anali kukhala ku Betaniya. Betaniya unali mudzi waung'ono womwe unali pafupi ndi Yerusalemu. Buku Lopatulika silimatiuza ife kuti ndiliti limene Yesu anacita ubwenzi ndi banja limeneli. Limatifotokozera kuti pamene Yesu ndi ophunzira ace anali kuyenda analowa m'mudzi ndikuti analandiridwa m'nyumba ya Marita ndi Mariya.

Pamene muyenda ulendo ndipo mukafika mu mzinda momwe bwenzi lanu limakhala, kodi mumacita ciani? Ndi zoona kuti inu mumapita ku nyumba yace. Cifukwa ciani? Mupita cifukwa mufuna kupereka moni kwa bwenzi lanu. Mupita cifukwa mudziwa kuti mukhoza kupeza cakudya kumeneko, ngati muli ndi njala. Mukhoza kupeza ciyanjano ndi cibwenzi. Mumakondwera mukamakhala pakati pa abwenzi.

Ndikhulupirira kuti zimenezi ndizo zifukwa zimene Yesu anapitira ku nyumba kwa Marita, Mariya ndi Lazaro.

GAWO LACIWIRI:

Tsegulani Buku Lopatulika lanu pa Luka 10:38-41. Werengani ndimezi. Pamene tinali kuwerenga ndimezo zinthunzi zina zinali kubwera m'malingaliro athu. Tikhoza kuona Marita pamene iye anali otanganidwa kwambiri. Kukonzera Yesu cakudya Mariya anali khale pa mapazi a Yesu. Iye ali kumvetsetsa ku ziphunzitso zace.

Posacedwa Marita alowa m'nyumba ndikuyamba kudandaulira Yesu za m'bale wace. Iye anati, "Kodi simusamala kuti mbale wanga

MUTU 11

PHUNZIRO LA GAWO: AZIMAI AM'BUKU LOPATU-LIKA

PHUNZIRO LALERO: MARIYA NDI MARITA

MAU A MULUNGU: Luka 10:38-42

MAU APAMTIMA: **"Muli abwenzi anga inu, ngati muzicita zimene ndinakulamulirani inu."**
**Yohane 15:14**

MTSOGOLERI:

Lero tiri kuphunzira phunziro losiliza la pa azimai a mu Buku Lopatulika. Tiri kuphunzira za akazi awiri amene anali pa cibale. Maina ao anali Mariya ndi Marita. Marita nthawi zonse anali otanganidwa ndi nchito za panyumba. Mariya anali cete ndipo anakonda kumvetsera ziphunzitso za Yesu pomwe anali kubwera kudzawacezera kunyumba yao.

Marita ndi Mariya anali ndi mbale wao dzina lace anali Lazaro. Yesu anali kukonda kuceza ku banja lao kwambiri. Yesu anakonda banja limeneli. Iwo anakonda Yesu ndipo anali kumucitira zinthu.

Pali maphunziro ena omwe tingaphunzire kucokera kuphunziro la Mariya ndi Marita.

GAWO LOYAMBA:

Marita ndi Mariya ali pa guru la azimai omveka mu Buku Lopatulika. Yesu anauza Marita poyamba kuti "Ine ndine kuuka ndi moyo; wokhulupirira ine, angakhale amwalira adzakhala ndi moyo, kodi ukhulupirira ici?" (Yohane 11:25-26).

Patangotsala masiku ocepa kuti Yesu apacikidwe, Mariya anazodza mapazi a Yesu ndi mafuta amtengo wapatali. Ndipo anthu



mukiremo. Anatuma mwana wace, Yesu Kristu, kudzafera macimo athu. Amationetsa njira ya cipulumutso. Iyi ndiyo nkhani yabwino imene tiyenera kugawana ndi anthu ena pa dziko lonse lapansi.

MTSOGOLERI:

Lero taphunzira za cikondi codabwitsa ca Mulungu. Taphunziranso kuti anthu onse kuli konse ali monga nkhosa zotaika. Aroma 3:23 atiuza kuti: "Onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu." Munthu ali yense ayenera kupulumutsidwa. Yesu afuna Mkristu aliyense kuti athandidze anthu osowa kuti amdziwe Iye. Tiyeni tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize kuti ife tiuze munthu wina za Iye, Sabata lino.

MUTU 2

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU

PHUNZIRO LALERO: WOFESA

MAU A MULUNGU: Mateyu 13:3-8, 18-23

MAU APAMTIMA: **"Ndipo zija za m'nthaka yokoma, ndiwo amene anamva mau nawasunga mu mtima woona ndi wabwino, nabala zipatso ndi kupirira."**
**Luka 8:15**

MTSOGOLERI:

Tikumbukira kuti Yesu anali kugwiritsa nchito mafanizo pophunzitsa zinthu zambiri kwa omutsatira ace. Anali kulankhula za zinthu zimene anthu anali kuzidziwa kwambiri. Lero phunziro lathu liri pa za wofesa ndi mbeu. Tonsefe timadziwa mbeu zofesa m'minda yathu. Conco, nafenso timadziwa za zinthuzi zimene Yesu anali kugwiritsa nchito mu nthano zimene analankhula kale kale. Fanizo limene tidzaphunzira lero limapezeka mu mabuku atatu a m'Cipangano Catsopano. Limapezeka mu Mateyu, Mutu 13, Marko, Mutu 4, ndi Luka, Mutu 8. Tidzawerenga ndime zina za

m'mabuku amenewa.

GAWO LOYAMBA:

Poyamba, tiyeni titsegure ma Buku Opatulika athu pa Mateyu Mutu 13. Tionanso kuti Yesu anali kulankhula za zinthu zimene anthu anali kudziwa bwino. (Werengani Mateyu 13:3.) Tingaone wofesa ali kutenga mbeu zace napita kukafesa. Pamene anali kufesa, mbeuzo zinagwa pa nthaka zosiyanasiyana. Zina mwa mbeuzo zinagwa pa njira. Mbalame zinabwera ndi kudya mbeuzo. Zina mwa mbeuzo zinagwera pa nthaka imene inali pamwamba pa miyala. Pamene mbeuzo zinayamba kumela, mizu yace siikanatha kulowa pansi kwambiri cifukwa cakuti pansi sipanali pakuya kwambiri. Zina mwa mbeuzo zinagwa pamene minga inali kumela. Pamene mbeu zinali kukula, mingayo inayamba kuziononga. Ndipo mbeu zina zinagwa pa nthaka yabwino. Mbeuzi zinabala zipatso zabwino.

Timadziwa za nthaka zamitundu imeneyi lero. Tingamvetse bwino cimene cimacitika ngati mbeu zikugwa panthaka yosiyana tere. Ndiponso timadziwa kuti cimanga cikafesedwa pa nthaka yabwino, tidzakolola cimanga cambiri.

Atasiriza kunena fanizo limeneli kwa ophunzira ace, Yesu anati, "Iye amane ali ndi makutu, amve" (Mateyu 13:9).

GAWO LACIWIRI:

Ophunzira anamfunsa Yesu, "Kodi cifukwa ninji m'malankhula nawo m'mafanizo? (Mateyu 13:10) Yesu anapereka zifukwa ziwiri zimene anali kulankhulira m'mafanizo. Cifukwa coyamba cinali cakuti nthano za mafanizo zinathandiza ophunzira ace kukumbukira bwino zinthu zimene ankafuna kuti awaphunzitse. Cifukwa cina cinali cakuti anthu amene anali adani ace sakanatha kumvetsa tanthauzo la ziphunzitso zace.

GAWO LACITATU:

Pomwe atatha kuwauza zifukwa zimene anali kulankhulira



Tsiku lina Yesu anali kuphunzitsa, mkazi wina mu gurumo ananena mau okweza kuti, "Yodala mimba imene idakubalani, ndi mawere amene munayamwa" (Luka 11:27). Yesu anayankha nati, "Inde, koma odala iwo akumva mau a Mulungu, nawasunga " (Luka 11:28). Mau amenewa ali aife lero. Iye anati pomwe titamva mau ace ndi kuwacita, tiri odala koposa mai wace Mariya.

Tiyeni tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize kumvetsetsa mau ace. Mupempheni kuti atithandize ife kuti tidzicita zimene mau ace amatiuza kuti tidzicita.

PEMPHERO:

GAWO LACINAI:

Mariya analipo pamene Yesu anacita zozizwitsa zoyamba (Yohane 2:1-11). Iye analipo pa nthawi imene Yesu anali kupacikidwa pamtanda (Yohane 19:25-27). Palibe buku la uthenga wabwino liri lonse lomwe limatiur a za m'mene Mariya anamvelera pomwe anaona Yesu ali kupacikidwa pamtanda.

Cisoni cace cinasandulika cimwemwe pamene Yesu anaukitsidwa kucokera kwa akufa. Mwina mwace pa nthawi iyi iye anayamba kumvetsetsa zinthu zonse zimene zinali kuonekera kwa mwana wace. Kawiri kawiri kanthu kena kakacitika timawerenga kuti, "koma Mariya anasunga mau awa onse, nawalingalira mumtima mwace" (Luka 2:19,51b). Iye anali ndi zinthu zambiri zoziganizira.

Yesu atapita kumwamba, omutsatira ace anabwerera ku Yerusalemu. "Iwo onse analikukangalika m'kupemphera, pamodzi ndi akazi, ndi Mariya amace wa Yesu, ndi abale ace omwe" (Macitidwe 1:14).

Sitiuzidwa zina za Mariya. Sitidziwa m'mene anafera ndi kuti anafa liti.

MTSOGOLERI:

Ife tikhoza kukhulupirira kuti Mariya anali mtsikana wabwino. Iye anali woyera m'moyo wace woyamba. Anakhulupirira Mulungu. Ndipo anafunitsitsa kucita cifuniro ca Mulungu m'moyo wace wonse.

Mulungu ali kufuna funa atsikana ndi azimai masiku ano kuti acite cifuniro cace m'miyoyo yao, kuti apindule anthu otaika, ndikuthandiza mpingo kuti ukule. Mulungu amafuna anthu odzicepetsa. Iye amafuna anthu amene ali ndi cikhulupiriro mwa Iye. Afuna anthu amene amafuna kucita cifuniro cace ngakhale kuti pakhale zotani. Ifenso monga Mariya tiyenera kudzipereka kwathunthu kucita cifuniro cace mu zinthu zonse.



mumafanizo, Yesu anauza ophunzira ace tanthauzo la fanizoli. Anati mbeu imene wofesa amafesa ndi mau a Mulungu. (Werengani Luka 8:11.) Anthu amene amamvera ku mau a Mulungu amalandira mauwo mosiyana. Conco anthu ali monga nthaka zosiyana. Yesu anati njira ili monga anthu ena amene amalandira mau a Mulungu. Koma Satana amabwera nacotsa mauwo m'mitima yawo kuti asakhulupirire ndi kupulumutsidwa.

GAWO LACINAI:

Nthaka ya pamwamba pa miyala iri monga anthu amene amamva mau a Mulungu ndipo amawalandira mokondwera. Koma mau a Mulungu samalowa kwambiri m'mitima yao. Pamene mabvuto abwera cifukwa ca mau a Mulungu, amatembenukira kwina. Minga ndi cithunzi ca munthu amene amva mau a Mulungu, koma iwo amasamala za moyo uno ndipo kukonda kwawo kwa cuma kumacotsa mau a Mulungu m'maganizo awo. Mau a Mulungu sabala zipatso mwa iwo. Nthaka yabwino iri monga anthu amene amamva mau a Mulungu ndipo amawasunga m'mtima wawo wabwino ndi womvera. M'moyo wotero mau a Mulungu angabale zipatso zambiri.

MTSOGOLERI:

Fanizo iri limaticenjeza ife tonse amene timamva mau a Mulungu. Tiyenera kukhala wosamala m'mene timverera uthenga wa Mulungu. Limalimbitsanso anthu onse amene amafalitsa uthenga wabwino, wa Yesu Kristu kwa anthu ena. Limatiuza ife kuti si anthu onse amene adzafuna kumva uthenga wa Yesu. Osati onse amene alandira uthenga wa Mulungu adzatsatira zinthu za Mulungu. Komabe, limatilimbitsa ife kukhulupirira kuti ngati tiri oona mukucitira Yesu umboni wathu, mau a Mulungu adzabeleka zipatso m'miyoyo ya anthu ambiri amene timacitira umboni.

Tiyeni tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize kuti tikhale okhulupirika polandira mau ace ndi pouza anthu ena za Iye.

Pemphero:

MUTU 3

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU

PHUNZIRO LALERO: MATALENTE

MAU A MULUNGU: Mateyu 25:14-30

MAU APAMTIMA: **"Mbuye wace anati kwa Iye, Cabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono, ndidzakhazika iwe pa zinthu zambiri; lowa iwe m'cikondwero ca mbuye wako."**

**Mateyu 25:21**

MTSOGOLERI:

Yesu anali mphunzitsi wamkuru kopambana amene anakhala padziko lapansi. Anali kugwiritsa nchito njira zambiri pofuna kuphunzitsa zoonadi za Mulungu. Kuphunzitsa m'mafanizo inali njira imodzi imene Yesu anali kugwiritsa nchito nthawi zambiri. Amene anali kumvetsera ku mafanizo anali kukumbukira bwino zimene Yesu anali kuwaphunzitsa. Masiku ano, pamene timvetsera ku nthano imene imaphunzitsa coona timakumbukira bwino coonadi. Fanizo la matalante liri ndi maphunziro ena kwa ife tonse lero monga momwe linali kuwakhuzira anthu akale aja.

GAWO LOYAMBA:

Tsegulani ma Buku Opatulika pa Mateyu 25. Tidzawerenga ndime zina kucokera pa mutu umenewu pamene tiri kuphunzira phunziro lathu lero. Ndime 14 ndi 15 zitiuza kuti munthu wina anali paulendo kupita ku dziko lina. Asanapite, anaitana akapolo ace atatu ndipo anawapatsa matalente. Kodi talente ndi ciyani? M'masiku a Yesu kunalibe ndalama monga zimene tiri nazo ife lro. Kunali cabe kulemera kwina kwa ndalama. Kucuruka kwa ndalamazo kukasamila pa mtundu wace monga kopa, golidi kapena siliva. Nthawi zambiri inali yopangidwa ndi siliva. Talente limodzi likanalingana ndi K500.00. Masiku ano timaganizira za matalente m'njira zambiri.



kwa Mariya ndi Yosefe kuti apite ku Betelehemu. Iwo anapita kumeneko kukalembetsa kwa kalembera. Ali komweko, Yesu anabadwira mkhola la ng'ombe, malo amene anali kusungiramo zoweta. Kodi inu muli kuganizira kuti Mariya anali wokondwa? Ine ndidziwa kuti Yosefe ndi Mariya analinso wokondwa. Timaudzidwa za abusa ndi anzeru aku m'mawa amene anapita kukawacezera ndi kukapembedza Yesu atangobadwa.

GAWO LACITATU:

Mariya ndi Yosefe anasamalira Yesu kwambiri. Yesu atangobadwa, mfumu Herode analamulira kuti ana onse acimuna a zaka ziwiri aphedwe. Mulungu anacenjeza Yosefe m'maloto kuti atenge Mariya ndi Yesu napite nawo ku Aigupto kukakhala. Iwo anakhala ku Aigupto kufikira kunali kwa ufulu kwa iwo kubwerera ku Nazareti.

Kodi inu muli kumbukira m'mene Yosefe anapitira ndi Yesu ku Kacisi ku Yerusalemu pomwe iye anali wa zaka khumi ndi ziwiri? Zinthu zonse zinayenda bwino kufikira iwo anayamba ulendo wobwerera kumudzi kwao. Pakumalizira kwa ulendo wa tsiku limodzi Mariya ndi Yosefe sanakhoze kupeza Yesu pakati pa anthu.

Kodi mwana wanu anasowapo kale kucokera pa nyumba yanu? Mai amakhoza kuganiza zinthu zambiri zomwe zingamucitikire. Iwo anafuna funa Yesu kwa masiku atatu asanamupeze. Iye anali mu kacisi. Pamene Yesu anadziwa kuti iwo anali kumufuna funa iye anati kwa iwo. "Kuli bwanji kuti munali kundifuna funa ine? Simunadziwa kodi kuti kundiyenera ine ndikhale m'zace za Atate wanga? (Luka 2:49). Mariya ndi Yosefe sanamvetsetse zomwe Yesu anabwerera nawo ku Nazareti ndipo iye anali kuwamvera iwo. "Ndipo amace anasunga zinthu izi zonse mumtima mwace" (Luka 2:51).

Yosefe anali kugwira nchito ya umisili wa matabwa. Inde, nayenso Yesu anaphunziranso nchito imeneyo. Buku Lopatulika limatiuza kuti "Ndipo Yesu anakulabe m'nzeru ndi mumsinkhu, ndi m'cisomo ca pa Mulungu ndi ca pa anthu" (Luka 2:52). M'njira yomwe ana athu masiku ano amakulira ndi momwe Yesu anakulira. Nditsimikiza kuti mkhalidwe kapena cikoka ca Mariya cinali cacikuru pa moyo wa Yesu.

nudzabala mwana wamwamuna, nudzamucha dzina lace Yesu" (Luka 1:30-31).

Yankho la Mariya linali funso. Iye anafunsa mngelo kuti, "Ici cidzacitika bwanji, popeza ine sindidziwa mwamuna? (Luka 1:34). Mngelo anamufotokozera kuti zidzatheka ndi mphamvu ya Mzimu Woyera kuti iye adzakhala mai wace wa Yesu. Yankho la Mariya lidaonetsa cikhulupiriro cace ca kwa Mulungu ndi kuonetsa kuti anafunitsitsa kumvera. "Ndipo Mariya anati, 'Onani,' mdzakazi wa Ambuye; kukhale kwa ine monga mwa mau anu" (Luka 1:38)

Timaciona kuti ndi cinthu cosamvetseka bwino ca za kabadwidwe ka Yesu, podziwa kuti iye analibe atate adziko lino lapansi. Luka 1:37 amanena kuti, "Palibe mau amodzi akucokera kwa Mulungu adzakhala opanda mphamvu" (Luka 1:37). Ndiye kuti cozizwitsa ca kubadwa kwa Yesu cinatheka ndi Mulungu.

GAWO LACIWIRI:

Pamene Mariya atangocezeredwa ndi mngelo anapita ulendo wautali kukacezera kwa mnansi wace Elizabeti. Mulungu anacitanso cozizwitsa cina m'moyo wa Elizabeti. Iye anali mai wokalamba yemwe anali pafupi kukhala ndi mwana. Mariya anakhala ndi Elizabeti kwa miyezi itatu.

Kodi inu mukhoza kuganizira za zinthu zomwe anali kunenera Mariya m'mene nthawi inali kupita? (Kuti mumvetsetse m'mene Yosefe anacitira za zinthu zomwe zinali kuoneka kwa Mariya. Werengani Mateyu 1:18-21.)

Yosefe amene anayenera kukhala mwamuna wodzamukwatira anaganiza zofuna kumukana. Komabe m'ngelo ndiye anadzalimbikitsa kuti "Pakuti ico colandiridwa mwa iye ciri ca Mzimu Woyera" (Mateyu 1:20b). Yosefe ndi Mariya anakwatirana. Ndipo sanakhalire malo amodzi monga mwamuna ndi mkazi kufikira Yesu anabadwa (Mateyu 1:25).

Nthawi yakubadwa kwa Yesu itayandikira, kunali kofunikira



Matalente ndi nzeru zimene Mulungu apatsa aliyense wa ife. Mulungu anapatsa aliyense wa ife kanthu kena kamene tingacite bwino pomutumikira. Anthu ena amaimba. Ena angaphunzitse. Ena angalalikire mau a Mulungu. Anthu ena angagwire nchito pamodzi ndi ana ang'ono ndipo angawaphunzitse zinthu za Mulungu. Kodi inu Mulungu akupatsani talante la mtundu wotani? Pezani talante lanu ndipo muligwiritsire nchito mu ulemerero wa Mulungu.

GAWO LACIWIRI:

M'phunziro lathu lalero taphunzira kuti munthu anapereka matalante kwa akapolo ace. Kwa m'modzi anapereka matalante asanu; kwa wina anapereka awiri; ndipo kwa winanso anapereka limodzi. Matalente amanewa anali kupatsidwa mofanana ndi momwe wolandilayo akanatha kuwagwiritsira nchito. Munthuyo anapita pa ulendo wace.

Tsopano tiyeni tione zimene akapolo anacita. Amene analandira matalente asanu anapindulanso ena asanu. Amene analandira matalente awiri anapindula awirinso. Koma uja amene analandira talante limodzi anakumba dzenje nalibisa momwemo.

Patapita nthawi yaitali, mbuye wao anabwera ndipo anaitana akapolo ace. Akapolo anafunsidwa kuti anene zimene anacita ndi matalente, amene anapatsidwa.

GAWO LACITATU:

Tinawerenga za akapolo awiri oyamba mu Mateyu 25:20 ndi 22. Amene analandira matalente asanu anapindulanso asanu. Conco anabweretsa matalente khumi kwa mbuye wace. Kwa onsewa mbuye wao anati, "Cabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono, ndizakhazika iwe pa zinthu zambiri; lowa iwe m'cikondwero ca mbuye wako " (Mateyu 25:21 ndi 23).

Koma nthano inasiyana kwambiri pamene kapolo wacitatu anabwera kwa mbuye wace. Asanabwere, anapita kukatenga talente kumene analibisa. Analikumba ndipo analibweretsa kwa mbuye wace.

Anayamba kudandaula. Anati, "Ndinakudziwani inu kuti ndinu munthu wouma mtima, wakututa kumene simunafesa, ndi wakusonkhanitsa kumene simunawaza, ndinaopa ine, ndinapita, ndinabisa pansi ndalama yanu: Onani, siyi yanu." (Mateyu 25:24-25)

Mbuye wace anali wokhumudwa kwambiri. Weremgani momwe anamuyankhira mu Mateyu 25:26-27. Pambuyo pace mbuye wace anati "Cotsani kwa iye ndalamayo, muipatse kwa amene ali nazo ndalama khumi" (Mateyu 25:28).

GAWO LACINAI:

Pali maphunziro ambiri amene tingaphunzire mu fanizo limeneli. Limatiuza ife kuti Mulungu amapatsa anthu mphatso zosiyana siyana. Mu nthanoyi munthu wina analandira matalente asanu, wina awiri, ndipo winanso limodzi. Kusiyana kwa kucuruka kwa matalente kunalibe kanthu. Comwe cinali cofunikira ndi momwe anthuwo anagwiritsira nchito matalente awo. Cimeneci cilinso coona lero. Mulungu amapatsa kwa aliyense wa ife nzeru zosiyana siyana, ndi mphatso zosiyana siyana, zomwe tingagwiritse nchito pomutumikira. Cofunikira kwambiri ndi cimene timacita nazo zinthuzo.

Fanizori limatiuzanso ife kuti mphatso yocita bwino nchito ndi kucita nchito yambiri. Ganizirani za akapolo awiri aja. Anacita bwino nchito yawo. Anali okhulupirika. Kodi mbuye wao anati, "mwacita bwino. Pitani mukapumure?" Iai, sanatero "Munali wokhulupilirika pa zinthu zazing'ono ndidzakhazika inu pa zinthu zambiri." Mateyu 25:21b ndi 23b. Tinganenenso kuti, mbuye anali kunena kuti, "Ndidzakupatsani nchito yambiri yocita." Mbuye anatenganso talente limodzi limene anali nalo kapolo wacitatu anapatsa kapolo amene anali matalente khumi.

Phunziro lina limene timaphunzira ndi iri. Ngati munthu alephera kugwiritsa nchito matalente ace adzatengedwa kwa iye. Ngati munthu adziwa kusema mithiko koma akana kutero, patapita zaka zambiri sazatha kusema bwino. Komabe, ngati asema



MUTU 10

| | |
|---|---|
| PHUNZIRO LA GAWO: | AZIMAI A M'BUKU LOPATULIKA |
| MUTU WALERO: | MARIYA, MAI WA YESU |
| MAU A MULUNGU: | Luka 1:26-31, 34-35, 37-38 |
| MAU APAMTIMA: | **"Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lace Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao." Mateyu 1:21** |

MTSOGOLERI:

Kwa nthawi yaitali kwambiri Ayuda anali kuyang'anira kubwera kwa Mesiya. Aneneri ananenera za kubwera kwace. Ngakhale Yesaya anena kuti, "Cifukwa cace Ambuye mwini yekha adzakupatsani inu cizindikilo; taonani namwali adzaima, nadzabala mwana wamwamuna, nadzabala mwana dzina la Imanueli" (Yesaya 7:14).

Lero tiphunzira za Mariya mai wa Yesu.

GAWO LOYAMBA:

Pamene Mulungu anayang'ana pa mtsikana yemwe akanakhala mai wa mwana wace, Kodi iye anasankhula mtsikana wa mtundu wotani? Iye tidziwa kuti anali namwali, kapena wa zaka makumi awiri. Iye anapalidwa ubwenzi ndi mwamuna dzina lace Yosefe. Iye anali kukhala mu mzinda wa Nazarete. Ine ndikhulupirira kuti iye anali kupembedza Mulungu ndipo anali kufuna kumacita cifuniro cace m'moyo wace.

Kodi mukhoza kungoganizira m'mene Mariya analiri pa tsiku limene m'ngelo Gabriel anaonekera kwa iye? Tamvani mau ace oyamba: "Wocitidwa cisomo, Ambuye ali ndi iwe" (Luka 1:28). Iye mwina anali ndi mantha cifukwa mngelo anena kuti, "Usaope Mariya; pakuti wapeza cisomo ndi Mulungu. Ndipo taona udzakhala ndi pakati,

GAWO LACISANU:

Kodi ndi maphunziro otani amene tingawaphunzire kucokera mu moyo wa Estere? Pamene Estere anali wamng'ono msuwani wace anamuphunzitsa kupemphera kwa Mulungu. Iye anakukhulupilira za ciphunzitsoco m'nyumba mwa mfumu. Maphunziro amene ife timaphunzitsa ana athu ndi ofunika kwambiri. Timayenera kukhala okhulupirika kuwaphunzitsa zinthu za Mulungu.

Estere anabvomereza kupereka moyo wace kuti apulumutse moyo wa anthu ace. Inu ndi ine mwina sitingafunsidwe kuti tipereke miyoyo yathu kupulumutsa wina wace. Koma Mulungu amatiyembekezera kuti tidzicita umboni kwa anthu otaika amene ali otizungulira. Cimeneci cimafunika kulimba mtima ndi cikhulupiriro. Iye amayembekezera kuti tidzipempherera anthu otaika, atsogoleri a dziko, mpingo ndi ana athu. Kodi inu mukhoza kucita zinthu zimenezi? Mau apamtima athu atiuza kuti Mulungu adzakhala nafe kuli konse komwe tiyenda. Iye adzatipatsa mphamvu ndi cilimbitso kuti timupembedze iye.

MTSOGOLERI:

Tiyeni tipemphe Mulungu kuti atithandize pamene tiri kuphunzitsa ana athu, kuti tidzicita bwino monga tingathere. Pemphani Mulungu kuti atipatse kulimba mtima pocitira umboni ena. Pemphani kuti atithandize kukhala okhulupirika konse komwe tiri ndi conse comwe ticita.

PEMPHERO:



mithiko yambiri, adzakhala wodziwa kwambiri.

Ndi cimodzi modzinso m'moyo wa Cikristu. Njira imodzi cabe yosungiramo matalente amene Mulungu anatipatsa ndi kugwiritsa nchito matalente amenewo mu nchito ya Mulungu ndi pothandiza anzathu.

MTSOGOLERI:

Taphunzira zinthu zambiri zodabwitsa mu fanizo la matalente. Tiyeni tikumbukire kuti kucuruka kwa matalente amene Mulungu amatipatsa kulibe kanthu. Cimene cifunika ndi njira zimene zikondweletsa Mulungu. Sitiyenera kukumba dzenje ndi kufocerapo matalente. Tiyenera kuwagwiritsa nchito ngati tidzawasunga.

Tiyeni tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atithandize ife kuti tikhale okhulupirika m'nchito yomwe timamgwirira masiku onse.

PEMPHERO:

MUTU 4

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU

PHUNZIRO LALERO: MKAZI WAMASIYE, NDI WOWERUZA WOSALUNGAMA

MAU A MULUNGU: Luka 18:1-8

MAU APAMTIMA: **"Comweco, ngati inu, muli oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akumpempha Iye?"**

**Mateyu 7:11**

MTOGOLERI:

Kodi m'mapemphera ndikuti m'maganizira kuti Mulungu sayankha mapemphero anu? Kodi m'makhumudwa ndi kuyamba kufunsa," ndi cifukwa ninji ndipitiliza kupemphera pamene Mulungu sandipatsa cimene ndifuna?" Kapena phunziro lathu lalero lidzakuthandidzani kuyankha mafunso okhuza pemphero.

GAWO LOYAMBA:

Fanizo la mkazi wa masiye ndi woweruza limapezeka cabe mu uthenga wabwino wa Luka. Luka asanayambe kunena nthano imene Yesu ananena, amafotokoza cifukwa cace cimene Yesu anawauzira ophunzira ace fanizo limeneri. Luka anati, "Ndipo anawanenera fanizo lakuti ayenera iwo kupemphera nthawi zonse, osafoka mtima" (Luka 18:1). Colinga ca fanizo limeneli cidzatithandiza ife kuti tione kuti tisafoke ngati tipemphera. Tiyenera kupitiriza kufuna funa cifunilo ca Mulungu ndi njira yace pa miyoyo yathu.

GAWO LACIWIRI:

Tiyeni tiyang'ane fanizo limeneli mu uthenga wa Luka, mutu 18. Tsegulani Buku Lopatulika ndipo mupeze ndime 1 kufikira 8. Fanizo iri litiuza ife za oweruza ndi mkazi wa masiye. Werengani



anawaitananso m'mawa mwace.

Pakati pa usiku mfumu Siinagone tulo. Ndipo anapita anayamba kuwerenga mabuku ambiri yakale. Iye adapeza nkhani ya m'mene Moredekai anapulumutsira moyo wace. Ndipo anaonanso kuti panalibe mphotho ina iliyonse yomwe Moredekai anailandira. Cidaoneka kuti Hamani anali kubwera pamaso pa mfumu kudzapempha kuti Moredekai apacikidwe.

GAWO LACINAI:

Ndipo mfumu inafunsa Hamani kuti kodi ndiciani cimene ciyenera kucitika kwa wina wace ngati mfumu itafuna kumulemekeza. Hamani anaganizira kuti munthuyo ndi iye! Motero iyė anapereka maganizo akuti munthuyo ayenera kubvala zobvala za mfumu. Iye adayenera kubvala korona ya mfumu pa mutu wace. Iye ayenera kubwera ndi buru wa mfumu poyenda m'miseu. Munthu adziyenda naye ndi kunena kuti, "Azitero naye munthu amene mfumu ikondwera kumcitira ulemu" (Estere 6:9, kumapeto kwa ndimeyo.)

Mfumu inalamulira Hamani kuti icitire Moredekai zinthu zonsezo. Kodi mukhoza kuona m'mene Hamani anakalipira? Atatha kucita zinthu zonsezi kwa Moredekai, Hamani anapita kukadya ndi mfumu ndi Estere. Ndipo pa cakudyapo, Estere anafotokozera mfumu zacidani cofuna kupha Ayuda. Mfumu inafuna kudziwa kuti ndi ndani anacita cinthu cotere. Pamene iye anayankha kuti, "Hamani," mfumu inakalipa kwambiri. Inacoka pa cakudyapo ndikupita m'munda. Pamene inabweranso, Hamani anali atagwa pansi pamaso pa mfumukazi. Ndipo mfumu poganizira kuti Hamani anali kufuna kucitira ciwembu mfumukazi, analamulira kuti Hamani apacikidwe.

Ndipo mfumu inauza Moredekai kuti alembe kalata ina. Ayuda anapatsidwa mwayi wokhoza kudzicinjiriza okha kwa anthu ofuna kuwapha patsiku laciweruzo. Imeneyi inali nthawi yacimwemwe kwa anthu a Ciyuda. Iwo anapulumutsidwa cifukwa ca kulimba mtima kwa Estere.

zinalembedwa mu bukuli kuphatikizapo dzina la Moredekai. Hamani anali munthu ogwira nchito mu bwalo la mfumu loweruzira milandu. Tsiku lina mfumu inapatsa Hamani gawo. Ndipo gawolo linamupanga iye kukhala onyada kwambiri. Iye analamulira kuti anthu adzimulambira. Moredekai anakana kuweramira Hamani cifukwa Ayuda anali kulambira Mulungu yekha. Cimeneci cinakalipitsa Hamani kwambiri. Ndipo mumtima mwace anafunitsitsa kupha Moredekai ndi anthu onse a Ciyuda. Ndipo iye anadandaula kwa mfumu kuti ibvomereze dongosolo la maganizo ace.

Hamani analemba kalata ndikuika cizindikiro ca mfumu. Kalatayo inati ayuda onse pa tsiku lina ayenera kuphedwa. Moredekai anali ndi cisoni kwambiri pamene anamva nkhaniyi. Estere mfumukazi ya tsopano inali pa cisoninso. Kumbukirani kuti iyenso anali Myuda, koma iye sanauze aliyense za zimenezi.

GAWO LACITATU:

Moredekai anatumiza uthenga kwa Estere, kupempha kuti iye apite kwa mfumu kuti afunse kuti apulumutse miyoyo yao. Estere anakumbutsa Moredekai kuti iye sakanakhoza kupita kwa mfumu pokha pokha ataitanidwa. Cifukwa cilango ca kuswa lamulo limeneli ndi imfa. Moredekai anamucenjeza kuti ngakhale iye anali mfumu yaikazi akanakoza kuphedwanso (Werengani Estere 4:13-14.)

Estere anatumiza mau kwa Moredekai kuti asonkhanitse pamodzi a Yuda onse amene anali kukhala mu mzindamo. Iwo ayenera kukhala osadya ndi kusamwa madzi kwa masiku atatu. Kuti apempherere Estere pa nthawi imeneyi. Ndipo Estere analonjeza kucita cimodzi modzi. Ndipo Estere analonjeza kuti adzapita pamaso pa mfumu. Tamvani mau ace olimbika, "Ndikaonongeka tsono ndiononongeke" (Estere 4:16, mau osilizira a ndimeyi.)

Estere anapita pamaso pa mfumu pa tsiku lotsiriza la citatu. Iye anamulora kuti abwere pamaso pace. Anafuna kudziwa kuti copempha cace ndi cotani. Estere anaitana mfumu ndi Hamani ku cakudya comwe anacikonza. Ndipo iwo anabwera. Ndipo



ndime 2. Kodi itiuza ciyani ca oweruza? Ikuti "wosaopa Mulungu, ndi wosasamala munthu " Luka 18:2b. Ici ndi cithunzi thunzi ca munthu woipa koposa.

Ndipo timaonanso mkazi wa masiye. Anali wofoka ndi wopanda cuma. Analibe munthu womuyang'anira. Anali ndi mabvuto ndi munthu wina. Sitidziwa kuti bvuto lace linali la mtundu wanji. Komabe, Buku Lopatulika litiuza ife kuti anali kupita kwa oweruza kumufunsa kuti amuthandize. Kwa nthawi ndithu anali kukana. Patapita nthawi anati, "Koma cifukwa ca kundibvuta ine mkazi wamasiye amene ndidzamweruzira mlandu, kuti angandilemetse ndi kudzaidza kwace " (Luka 18:5). Conco anabvomera. Pambuyo pace Yesu anafunsa funso nati, "Ndipo kodi Mulungu sadzacitira cilungamo osankhidwa ace akumuitana usana ndi usiku, popeza aleza nao mtima?" (Luka 18:7).

GAWO LACITATU:

Kodi fanizo iri litiuza ciyani ife? Kodi linena kuti Mulungu ali monga oweruza wosalungama? Iai sitero ai. Litiuza kuti oweruza wosalungama anabvomera kuweruza mulandu wa mkazi wa masiye cifukwa cakuti mkaziyo anapitilira kufunsabe.

Mulungu akonda ana ace. Afuna kuwapatsa zinthu zabwino. Amadziwa zimene tifuna ngakhale pomwe tisanamufunse. Komabe, amafuna kuti tidzilankhula naye pa zinthu zonse zomwe zikhuza miyoyo yathu. Ife amene tiri makolo timadziwa zinthu zimene ana athu amafuna. Timafuna kuti iwo adzitiuza zinthu zimene afuna. Cili cimodzi modzinso ndi Mulungu.

Fanizo iri silitiuza kuti Mulungu adzatipatsa zonse zimene tifuna kamba kakuti tikupitilidzabe kufunsa ai. Litiuza ife kuti tidzifunsabe cifukwa tidziwa kuti Mulungu adzamvera ndipo adzayankha monga mwa cikondi cace ndi nzeru zace. Mulungu nthawi zonse amayankha mapemphero athu. Koma nthawi zonse sakuti "Inde" ai. Ndi coona nthawi zina limakhala "iai." Nthawi zina yankho limakhala "yembekeza pang'ono." Nthawi zambiri ndi cinthu cabwino kuti Mulungu satipatsa zomwe timafunsa nthawi yomweyo tafunsira. Nthawi

zambiri sitimadziwa zinthu zabwino pa Iye. Koma Mulungu amadziwa.

GAWO LACINAI:

Mu gawo losilizira la Luka, mutu 17, Yesu anauza ophunzira ace za imfa yace pamtanda. Analankhulanso za ucimo m'dziko. Anawauza kuti anthu anakonda zinthu za pa dziko koposa zinthu za Mulungu. Ndi nthawi monga zimenezi zomwe zimabwezera kumbu-yo Akristu.

Yang'anani dziko lapansi lero. Timapeza anthu ambiri amene amaseka zinthu za Mulungu. Timaona anthu amene sali Akristu. Iwowa amaoneka wokondwa kwambiri. Amaoneka monga alibe mabvuto. Akristu amafoka ataona kuti anthu amene sali Akristu akupita patsogolo. Izi ndizo nthawi pamene tiyenera kukumbukira fanizori ndi ziphunzitso zace.

MTSOGOLERI:

Tinafunsa mafunso awiri poyambira pa phunziro lathu. Tiyeni tiganidzirenso za mafunso amenewo. Kodi inu mumapempheradi ndipo m'manena kuti Mulungu sakuyankhani mapemphero anu? M'makhumudwa ndipo m'mafunsa "Ndipempheranji ngati Mulungu wandipatsa zomwe ndimafuna?" (Patsani nthawi azimai kuti alankhulepo pa mafunso amenewa.)

Imakhalapo nthawi pa moyo wa Mkristu ali yense pamene adzayankha, "Inde" kumafunso onse awiri. Ici ndi cifukwa cakuti ife tiri anthu. Phunziro lathu lero latiuza kuti Mulungu nthawi zonse amayankha mapemphero athu molingana ndi cikondi cace ndiponso nzeru zace. Kumbukirani kuti nthawi zonse sakuti, "Inde" ai. Nthawi zonse samayankha titasiliza cabe kupemphera ai.



**a Ciyuda. Mulungu anatsogolera anthu a ku dziko la malonjezano, atakomana ndi mabvuto ndi mayesero ambiri. Patapita zaka zambiri, anthu a Ciyuda anacimwira Mulungu koposa. Potsilizira Mulungu analora mitundu ina kuti ibwere ndikuwagonjetsa iwo nabalalitsidwa m'maiko ambiri. Ndipo inali nthawi imeneyi pomwe nkhani ya Estere inacitika.**

**GAWO LOYAMBA:**

**Estere ndi anthu ambiri ena a Ciyuda anali kukhala m'dziko la Perezi. Ahaswero anali mfumu ya dziko lalikuru.**

**Cinaoneka kuti mfumu inali kupatsa phwando lalikuru kwa anthu ambiri. Iye anaitanitsa mkazi wace Vasiti. Mkazi anakana kuka-onekera pamaso pa mfumu. Cimeneci cinamukalipitsa kwambiri. Mfumu inalankhula poyera kuti mkazi wace sadzakhalalanso mfumu yaikazi. Iye anaganizira kusankhanso mkazi wina kuti akhale mfumu yaikazi.**

**Atsikana onse okongola anaitanidwa kunyumba ya mfumu. Colinga cakuti pakapita kanthawi wina adzasankhidwa kuti akhale mfumukazi. Moredekai, msuwani wace wa Estere, analimbikitsa Estere kuti apite kunyumba ya mfumu. Estere anauzidwa kuti sayene-ra kuulura kuti iye ndi Myuda.**

**Ife timauzidwa kuti Estere "anayamikizidwa pamaso pa onse ompenya" (Estere 2:15b). Pamene nthawi inakwana yoti apite pamaso pa mfumu Ahaswero, timawerenga kuti "ndipo mfumu inakonda Estere koposa akazi onse, nalandira iye kuyanja ndi cifundo pamaso pace, koposa anamwali wacifumu pamutu pace, namuyesa mkazi wamkuru m'malo mwa Vasiti" (Estere 2:17)'**

**GAWO LACIWIRI:**

**Tsiku lina Moredekai anali kukhala pa cipata ca nyumba ya mfumu ndipo iye anamva za dongosolo lofuna kucotsa mfumu. Ndipo iye anadziwitsa Estere za cinthuci ndipo iye anacenjeza mfumu. Anthuwo analangidwa atatha kufufuza za dongosolo lao. Zinthu zonsezi**

okhulupirika mzinthu zonse.

PEMPHERO:

MUTU 9

PHUNZIRO LA GAWO: AZIMAI A M'BUKU LOPATULIKA

MUTU WALERO: ESTERE

MAU A MULUNGU: Estere 4:14

MAU APAMTIMA: **"Kodi sindinakulamulira iwe? khala wamphamvu, nulimbike mtima, usaope, kapena kutenga nkhawa, pakuti Yehova Mulungu wako ali ndi iwe kuli konse umukako."**
**Yoswa 1:9**

MTSOGOLERI:

Lero tiri ndi nthano yokondweretsa ya Estere mu phunziro lathu. Inu mukhoza kuwerenga buku la Estere kunyumba. Kumbukirani kuti mu Buku Lopatulika muli mabuku awiri omwe ali ndi maina a akazi. Iwo ndi Rute ndi Estere. Mabuku onsewa ali mu Cipangano Cakale.

Pamene ucimo unalowa m'dziko kupyolera mu kusamvera Mulungu kwa Hava, Mulungu analonjeza kuti iye adzatumiza Mpulumutsi. Patapita nthawi yaitali, Mulungu anasankha Abrahamu kuti akhale atate a anthu ace. Iye analonjeza kuti mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa kupyolera mwa Abrahamu. Yesu adayenera kubadwa kucokera ku banja la ana a Abrahamu.

Pamene nthawi inali kupita, banja la Abrahamu linakhala mtundu waukuru. Iwo anali kuchedwa ana a Israyeli kapena anthu



Tiyeni tifunse Mulungu kuti atipatse nzeru kuti tipemphere pemphero limene lizamkondweretsa.

PEMPHERO:

MUTU 5

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU

PHUNZIRO LALERO: MUNDA WA MPHESA NDI OLIMA MUNDA

MAU A MULUNGU: Luka 20:9-19

MAU APAMTIMA: **"Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika mthupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa."**
**2 Akorinto 5:10**

MTSOGOLERI:

Yesu ananena mafanizo ambiri pamene anali pansi pano. Mafanizo anali kuthandiza ophunzira ace kuti akumbukire bwino zoonadi za Mulungu. Taphunzira kale mafanizo anai taphunzira zinthu zambiri zodabwitsa zokhuza Mulungu ndi cikondi cace pa anthu onse. Lero tidzaganizira za m'mene ife timayankhira ku cikondi ca Mulungu ndi madalitso ace.

GAWO LOYAMBA:

Pamene Yesu anali padziko lapansi, malo amene anali kukhalako nthawi zina anali kukhala ndi eni ace amene sanali kukhala pa malowo. Anthuwa anali kusiira anthu ena minda yao. Anthuwa anali kuwalipira ena minda ndi zokolola zao. Nthawi zambiri anali kugawana pakati

zokololazo.

Amene anamvetsera ku fanizo limeneli anamvetsetsa zomwe Yesu anali kutanthauza ndi fanizoli. Kodi mukumbukira mu phunziro laciwiri, tinaphunzira cifukwa cimene Yesu anali kulankhulira mu mafanizo. Cifukwa cinali cakuti anthu amene anali adani ace asamve tanthauzo la zophunzitsa zace. Angakhale adani a Yesu anamva tanthauzo la fanizo ili. (Werengani Luka 20:19.)

GAWO LACIWIRI:

Tsegulani Buku Lopatulika pa Luka 20:9-19.

Nthano imene ananena Yesu inali iyi. Munthu analima munda wa mphesa. Anapangana ndi anthu ena kuti aziyang'anira mundawo. Pambuyo pace anapita ku dziko lakutali kumene anakhala nthawi yaitali. Anadziwa nthawi yokolola. Oyang'anira munda sanapatse akapolo kanthu kali konse. Coona cinali cakuti oyang'anira munda anali kuwazunza akapolo. Izi zinali kucitika nthawi zambiri.

Posirizira mwini munda anatuma mwana wace kwa oyang'anira, ali kuganizira kuti iwowa adzamuopa mwanayo. Anapha mwana wa mwini munda. Pambuyo pace Yesu anafunsa, "Pamenepo mwini munda wamphesawo adzawacita ciani? Iye sadzafika nadzaononga olima munda aja nadzapatsa munda kwa ena " (Luka 20:15b-16).

GAWO LACITATU:

Tanthauzo la fanizoli ndi lapafupi. Mwini munda wa mphesa ndi Mulungu. Munda wa mphesa unali mtundu wa Israyeli. Olima munda anali oweruza a Israyeli kwa amene dzikoli linapatsidwa. Akapolo amene anatumidwa kwa olima munda anali aneneri amene anazunzidwa ndi kuphedwa. Mwana wa mwini munda anali Yesu. Imfa ya mwanayo inali imfa ya Yesu, pa mtanda, imene inali pafupi. Cilango ca olima munda oipa cinali cakuti Ayuda sankakhalanso okha osankhidwa a Mulungu ai. Malowo akanapatsidwa kwa anthu ena.



Kodi ndi maphunziro ena otani amene tingawaphunzire kucokera ku umoyo wa Rute? Naomi ndi a pabanja lace anali kupembedza Mulungu woona ndi wamoyo. Iwo anapita kukakhala pakati pa anthu aku Moab. Anthu amenewo anali kupembedza mafano. Ana a Naomi anakwatira akazi a ci Moab. Ife tikhoza kukhulupilira kuti cinali cifukwa ca mkhalidwe wabwino wa Naomi ndi banja lace kuti Rute anakhala otsatira wa Mulungu woona ndi wamoyo.

Pamene Naomi anabwerera ku dziko la kwao, Rute anasankha kusiya dziko lace ndi kupita ndi mpongozi wace. Tamvani mau acikondi amene Rute analankhula (Werengani Rute 1:16-17.) Iye anasankha kukhala okhulupirika kwa Mulungu. Mulungu amayembekeza kuti Mkristu aliyense masiku ano akhale okhulupirika kwa Iye. Cikhoza kukhala ngati cinthu cobvuta, koma Mulungu adzatipatsa mphamvu ngati tifuna kukhaladi okhulupirika.

Moyo wa Rute ndi kukhulupirika kwace potsata Mulungu zinali umboni wabwino kwa Boazi. Iye anali atamva za Rute ndi cifundo cace kwa Naomi. Motero iye anacitira Rute cifundo. Mulungu anadalitsa Rute m'njira zodabwitsa zambiri. Leronso pamene tikhala okhulupirika kwa Mulungu ndi kufuna kucita cifuniro zace, Mulungu amatipatsa madalitso ambiri.

MTSOGOLERI:

Mulungu akhoza kukuitanani kopanda kukusiisani banja lanu ndi dziko lanu kuti mumtsate Iye. Komatu iye amayembekeza Mkristu aliyense kukhala okhulupirika. Ife tikhoza kukhala okhulupirika kwa Mulungu m'mabanja athu. Tikhoza kukhala okhulupirika pophunzitsa ana athu zinthu za Mulungu. Tikhoza kukhala okhulupirika mu ciyanjano cathu ndi mwamuna wathu. Ife tikhoza kucita bwino nchito imene Mulungu watipatsa kuti tiicite. Pamene ife ticita zinthu izi, Mulungu adzatidalitsa ndi kutithandiza kuti tikhale mdalitso m'miyoyo ya anthu ena. Kumbukirani mau apamtima athu: "Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo " (Afilipi 4:13).

Tiyeni tithokoze Mulungu cifukwa ca nkhani ya Rute. Tiyeni tipemphere ndi kufunsa Mulungu kuti atipatse mphamvu yokhalira

anamupempha kuti atsalire kuti atengenso cakudya m'mundamo. Anamupatsa cilolezo cakuti akhoza kumwa nao madzi amene anchito ace anali kumamwa. Pamene Rute anafunsa kuti kodi ndicifukwa ciani anali kucitiridwa cifundo conseci iye anayankha kuti, "Anandifotokozera bwino zonse zomwe unacitira mpongozi wako atafa mwamuna wako; ndi kuti wasiya atate wako ndi mako, ndi dziko lobadwirako iwe, ndi kudza kwa anthu osawadziwa iwe kale. Yehova akubwezere nchito yako, nakupatsa mphotho yokwanira Yehova, Mulungu wa Israyeli, amene unadza kuthawira pansi pa mapiko ace" (Rute 2:11-12.)

Pamene iye anabwerera m'madzulo Rute anali ndi ngala za tirigu wambiri. Naomi anali wokondwa kuti Rute anagwira nchito m'munda wa Boazi. Ndipo Naomi anauza Rute kuti Boazi anali m'modzi wa pabanja lao. Nthawi itapita, Naomi anafunitsitsa kuti Rute adayenera kukhala ndi nyumba yace. Potsatira mwambo wa nthawi imeneyo, Naomi anauza Rute kuti apite kwa Boazi kuti akathandize nchito.

Rute anacita monga momwe Naomi anamuuzira. Boazi anamuuza kuti iye akanakhala okondwa kucita cinthu cotere, koma anati panali wina wace amene anali m'nansi wao weni weni woposa iye. Iye analonjeza kuti akalankhula ndi munthu ameneyo ndikumufunsa ngati anali kufuna kukwatira Rute.

GAWO LACINAI:

Tsiku lotsatira Boazi anapeza m'nansi uja namufotokozera za Rute. Munthu uja anakana kuti sakanakhoza kulowa cokolo kwa Rute. Cinthu cimeneci cinapatsa mpata Boazi kuti akhoza kukwatira Rute (Werengani Rute 4:9-10.)

Motero Rute ndi Boazi anakwatirana. Patapita nthawi, Mulungu anawapatsa mwana. Anamucha Obedi. Pamenepo Naomi anakhala okondwa. Ndipo Obedi anakhala gogo wa mfumu Davide. Makolo ace a Ambuye Yesu analembedwa mu Mateyu, mutu 1. Timapeza maina a Rute ndi Boazi mu mutu umenewu (Werengani Mateyu 1:5.)



Tsopano onani ndime 19. Itiuza kuti ansembe ndi alembi anadziwa kuti Yesu anali kunena iwo.

GAWO LACINAI:

Fanizoli linali ndi uthenga kwa anthu amene analiko pa nthawi imeneyo. Kodi linena ciani kwa ife lero? Mufanizoli tinaphunzira kuti munda wamphesa unakonzedwa ndi mwini munda ndipo unapatsidwa kwa olima. Mulungu anakonza dziko lino m'mene tikhala. Anatipatsa moyo, mathupi abwino, mphamvu ndi madalitso ena ambiri. Anatipatsa mwana wace Yesu Kristu. Tidziwa uthenga wa cipulumutso mwa Yesu Kristu. Kodi ticita ciani ndi onsewa? Kodi ticita ciani ndi Yesu?

Olima anacimwira mwini munda wamphesa. Anakana kumpatsa mwini zomwe zinali zace. Anakana amithenga a mwini. Anapha mwana wace.

Munthu angacimwire Mulungu mu njira zoterezi angakhale lero. Angakane kumuika Yesu kuti akhale oyamba m'moyo wace. Anganene "Iai" kwa Yesu monga mbuye ndi Mpulumutsi. Pamene munthu akuti "Iai" kwa Mulungu pofuna kucita cifuniro cace, uja ndi ucimo.

Mufanizori, nthawi inabwera yoti olima adzinenele zomwe anacita. Cimodzi modzinso ndi ife lero. Tidzaitanidwa kukadzinenera milandu yathu kwa Mulungu pa zomwe timacita ndi madalitso amene anatipatsa.

MTSOGOLERI:

Ndi udindo wathu monga Akristu kukhala okhulupirika kwa Mulungu mu zinthu zonse. Mulungu ayenera kukhala woyamba m'miyoyo yathu. Tiyenera kudzindikira kuti Mulungu ndiye mwini zonse. Anatipatsa madalitso ambiri: Madalitso a moyo, kukhala opanda matenda, mphamvu, nzeru, ndi enanso ambiri. Mu zonse zimene timacita tiyenera kuyesayesa kukondweretsa Mulungu. Tikatero tidzakhala oyang'anira abwino a zinthu zomwe Mulungu anatipatsa.

Tiyeni tifunse Mulungu kuti atipatse nzeru kuti tikhale

oyang'anira abwino a zonse zimene anatipatsa.

PEMPHERO:

MUTU 6

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU

PHUNZIRO LALERO: MWINI CUMA WOPUSA

MAU A MULUNGU: Mateyu 6:19-21

MAU A PAMTIMA: **"Pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso."**
**Mateyu 6:21**

MTSOGOLERI:

Kodi ndi ciani cimene cimapangitsa munthu kuti akhale wopambana? Kodi ndi kucuruka kwa malo olimapo, zokolola zabwino, nyumba yaikulu, maphunziro abwino, cakudya cambiri, kapena cuma cambiri? Anthu ena amaganizira kuti munthu akakhala ndi zinthu zotere ali wa mwai kwambiri. Amaganizira kuti anthu amene ali ndi zinthu zotere ali ndi moyo wabwino. Phunziro lathu lero lidzatiuza zimene Yesu ananena kuti zimapatsa moyo wabwino.

GAWO LOYAMBA:

Tsegulani Buku Lopatulika pa Luka 12:13-21. Koyambirira kwa mutu 12 timaphunzira kuti anthu ambiri anabwera kudzamvetsera zomwe Yesu anali kuphunzitsa. Yesu anacenjeza ophunzira za mabvuto omwe akanawabwelera kamba kokhulupirira Yesu.



Elemeleki anali kukhala m'Betelehemu. Ndipo cakudya cinali mdziko la Moab. Motero Elimeleki, mkazi wace Naomi, ndi ana amuna awiri anapita kukhala mdziko la Moab. Atangofika kumeneko, Elimeleki adafa. Ndipo anao anakwatira akazi a m'dziko la Moab. Akaziwo maina awo anali Rute ndi Olipa. Patapita zaka khumi ana a Naomi adafa. Ndipo Olipa ngakhale Rute analibe ana.

Naomi anayamba kufuna kubwerera kumudzi kwao. Pamene iye anakonzekera za ulendo Rute ndi Olipa anamuperekeza pa njira. Ndipo Naomi adapempha apongozi acewo kuti abwerere kwa makolo ao. Poyamba onse anakana. Iye anapitirira kuwadandaulira. Potsiliza Olipa anabwerera kwa amai ace. Koma Rute anakanabe. (Werengani zomwe Rute ananena kwa mpongozi wace mu Rute 1:16-17.) Ndipo iwo anapitiriza ulendo wautaliwo ali pamodzi, kufikira iwo anafika ku Betelehemu.

GAWO LACIWIRI:

Naomi anali atapita ku Moabu ndi mwamuna, ndi ana ace awiri. Tsopano anali kubwerera ndi mpongozi wace mkazi yekha. Iye anali wosakondwa ndiponso wopanda womsangalatsa.

Rute anali mlendo m'dziko lina. Kodi inu munayamba mwakhala patali ndi ku mudzi kwanu ndi banja lanu? Kodi inu munali kumva bwanji? Rute anakonda mpongozi wace wamkazi kwambiri. Rute anafuna kumusamalira iye. Rute anapempha Naomi kuti amulore kuti apite m'minda kuti akatengeko cakudya cotsalira kuti azidya. Naomi anamulora kuti apite.

Nthawi imeneyo unali mwambo wakuti anchito akanasiya pang'ono cakudya m'malo ena a mundawo ndi kumapeto kwa m'nzere uli wonse. Anthu osauka anali kubwera ndi kudzatenga cakudya cotsaliraco. Njira imeneyi ndi yomwe ambiri anapezeramo cakudya.

GAWO LACITATU:

Pamene Rute anapita kukatenga cakudya cotsalira m'minda, cidaoneka kuti iye anapita m'munda wa Boazi. Boazi anamuona Iye. Iye anafunsa kuti kodi mlendoyu ndi wakuti? Anauzidwa kuti iye anali wa ku Moab ndipo anabwera ndi Naomi.

Boazi anali wacifundo kwambiri tsiku limenelo kwa Rute. Iye

MUTU 8

PHUNZIRO LA GAWO: AZIMAI AM'BUKU LOPATULIKA

PHUNZIRO LALERO: RUTE

MAU A MULUNGU: RUTE 1:16-18

MAU APAMTIMA: **"Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo."**
**Afilipi 4:13**

MTSOGOLERI:

Lero tiyamba kuphunzira za azimai anai a mu Buku Lopatulika. Azimai awiri anakhala m'nthawi ya mu Cipangano Cakale. Azimai awiri ena anakhala m'masiku a Yesu.

Pa nthawi ya Buku Lopatulika azimai anali ndi malo otsika m'moyo. Mkazi anali kuganiziridwa kuti ndi m'modzi wa akatundu amwamuna. Mkazi wa masiye sakamakhoza kupeza katundu wosalira kukhala. Umenewu unali mwayi wa ana amuna. Kale kale mu Israyeli, ngati mwamuna afa opanda ana, inali nchito ya acibale amwamunayo kukwatira mkazi wamasiyeyo.

Inali nthawi imene zinthu za mwambo zimenezi zinali kucitika mu Israyeli pamene nkhani ya Rute idacitika. Ife tikhoza kuphunzira maphunziro ena kucokera m'moyo wa Rute.

GAWO LOYAMBA:

Buku la Rute limapezeka mu Cipangano Cakale. Ndi Buku locepa, liri ndi mitu inai yokha. Cikhoza kukhala cinthu cabwino kuliwerenga sabata lino kunyumba nthawi ina. Mukhoza kumvetsetsa bwino zinthu zimene tiri kuphunzira lero poliwerenga bukuli.

Rute sanali wa ci Israyeli. Iye anali kukhala m'dziko la Moab. Ndipo m'dziko la Yuda munali njala yaikuru. Munthu wina ochedwa



Pamenepo munthu wina analankhula. Anali wodankhawa ndi cuma. Anati, "Mphunzitsi, uzani mbale wanga agawane ndi ine cuma camasiye " (Luka 12:13b). Yesu anakana kukhala oweruza pakati pa munthuyo ndi mbale wace. Pambuyo pace Yesu ananena cinthu cina cokondweretsa kwambiri. Anati, "Cifukwa moyo wace wa munthu sulingana ndi kucuruka kwa zinthu zace ali nazo" (Luka 12:15b).

Yesu anagwiritsa nchito fanizo pofuna kuonetsa anthu tanthauzo la mau ace. Panali munthu wina wa cuma amene anakolola cakudya cambiri mu munda mwace. Anayamba kuganizira zocita. Nkhokwe zace zinali zodzala. Sizinali zazikuru kwambiri kuti zokolola zonse zikanatha kulowamo. Anaganizira zoti apasule nkhokwezo, ndi kumanganso. Anati, "Ndipo ndidzati kwa moyo wanga, moyo iwe, uli naco cuma cambiri cosungika kufikira zaka zambiri tapumulatu, nudye, numwe, nukondwere" (Luka 12:19). Anaganidzira kuti sakanagwiranso nchito kwa zaka zambiri. Conco akanapumula nakondwera.

Anali kuganizira cabe za mwini yekha. Anaiwala kumuthokoza Mulungu kamba ka zinthu zonse zabwino zimene anali nazo. Anaiwalanso kuthandidza anthu osowa. Mulungu anati kwa Iye. "Wopusa iwe, usiku womwe uno udzafunidwa moyo wako, ndipo zinthu zimene unazikonza zizakhala za yani?" (Luka 12:20).

Yankho loonekeratu ku funso lija linali lakuti munthu uja sakanatha kupita nazo zinthuzo atamwalira. Munthu wina ankazitenga. Zinthu zomwe anadzikonzera iye mwini zinkagwiritsidwa nchito ndi munthu wina.

GAWO LACIWIRI:

Tingaganizire, "Munthu uja anali ndi cuma cambiri sanali kuda nkhawa ndi kanthu kali konse." Mulungu sanaganizire kuti munthuyu anali wacuma. Mulungu anati anali wopusa.

Kodi ucimo wace unali wakuti anali ndi cuma cambiri? Iai. Ucimo wace unali wakuti analephera kucita kanthu kena ndi cuma cace. Anali kudziganizira za iye mwini cabe. Sanaganizire za Mulungu kapena anthu ena. Sanaganizire zogawana cuma cace ndi

anthu ena amene anali kusowa.

Lero, lino ndi yeselo lalikuru pa anthu ambiri. Timaganiza kuti ngati munthu ali ndi zinthu zambiri ali ndi cuma. Akristu ambiri ali kuganizira zolandira ndalama zambiri kapena kupeza katundu wambiri. Ndi ang'ono amene aganizira zopereka gawo la ndalama zao ku nchito ya Mulungu. Ngati Mkristu aliyense akanatha kucita zomwe Yesu anaphunzitsa zokhuza cuma cao, dziko lino likanakhala labwino.

GAWO LACITATU:

Kodi Yesu aphunzitsa ciani za cuma? Yang'anani pa Mateyu 6:19-21. Yesu anauza ophunzira ace kuti kunali kupusa kudzikundikira cuma pansi pano. Cuma cotere cikanatha mosacedwa. Cikanacotsanso maganizo a munthu pa Mulungu.

Ndilikudziwa anthu ena amene analibe zambiri. Anali kubwera ku chalichi ndipo anali kuoneka monga Akristu okhulupirika. Anayamba kulandira ndalama zambiri. Posacedwa anasiya kubwera ku chalichi. Nthawi yao yonse anali cabe kuganizira za kulandira ndalama zambiri. Kodi mukudziwa munthu wotere? Cifuno copeza ndalama zambiri cinabwera pakati pa anthuwo ndi Mulungu.

Yesu aticenjeza kuti tisadzikundikira cuma pansi pano. Koma ngati tadzikundikira cuma kumwamba sicingataike. Kodi ici citanthauza kuti tisagwire nchito ndi kupeza cakudya, zobvala ndi maphunziro abwino? Iai, ici sicimene Yesu ali kuphunzitsa.

Akuti "cifukwa cace ndinena kwa inu, musadere nkhawa moyo wanu cimene mudzadya ndi cimene mudzamwa; kapena thupi lanu cimene mudzabvala. Kodi moyo suli woposa cakudya, ndi thupi loposa cobvala?" (Mateyu 6:25). Mulungu adziwa kuti timafunika zonsezo. Yesu analonjeza kuti ngati timaika Mulungu ndi cifuniro cace poyamba m'miyoyo yathu, Mulungu adzatipatsa zinthu zomwe tifuna (Werengani Mateyu 6:33.)



Lero tamaliza maphunziro a mafanizo a Yesu. Yesu analankhula mafanizo ambiri. Tangophunzira asanu ndi awiri okha aiwo.

Taphunzira kale zinthu zambiri zomwe zidzatithandiza ife pa moyo wa Cikristu. Poyamba tinaphunzira kuti munthu wopanda Yesu Kristu ali wotaika. Ndipo tinaphunzira kuti tiyenera kukhala osamala za njira imene tingamverere uthenga wa Mulungu. Timayenera kulandira ndi mitima yathu monga mbeu imene inagwa pa nthaka ya bwino

Kaciwiri tinaphunzira kuti Mulungu amapatsa aliyense wa ife matalente ena. Njira imene timagwiritsira matalentewa ndi yofunika kwambiri. Mulungu amatiyembekezera kuti ife tidziwagwiritsa nchito yotumikira Iye.

Fanizo la za mkazi wa masiye ndi oweruza limatilimbikitsa ife kukhala okhulupirika m'mapemphero a Mulungu. Mulungu amayankha mapemphero athu molingana ndi cikondi ndi nzeru zace. Ndipo tinaphunziranso kuti Mulungu amatipatsa ife madalitso ambiri. Iye amayembekeza kuti ife tikhale osamalira bwino madalitso amenewa.

Mphunziro la sabata lapita tinaphunzira kuti Mkristu ayenera kuika Mulungu m'moyo wace coyamba. Njira imeneyi ndi imene tingakhalire wopambana pamaso pa Mulungu.

Lero taphunzira kuti Yesu adzabweranso. Tiyenera kukonzekera tsopano za kubweranso kwace kwaciwiri. Pamene tidzafika pa nthawi ya imfa sitidzatha kukonzekera.

Tsopano tiyeni tipemphere ndi kuthokoza Mulungu cifukwa ca maphunziro amene tawaphunzirawa. Tiyeni timupemphe molingana ndi cifuniro cace. Pemphani Mulungu kuti atipatse kulimba mtima ndi mphamvu kuti tikhoza kugawira ena uthengawu kwa anthu otaika.

PEMPHERO:

wace. Iye ayenera kukhala moyo monga wa Yesu. Mau a Mulungu amatiuza ife m'mene tingakhalire ndi moyo wa Cikristu. Motero, powerenga Buku Lopatulika ndi kupemphera tikhoza kudziwa m'mene tingakhalire moyo wokondweretsa Yesu. Njira zimenezi ndi zimene tingakonzekere za kubweranso kwa Yesu Kristu.

GAWO LACITATU:

Kodi ndi maphunziro ena otani amene timawaphunzira kucokera m'fanizoli? Kodi pamene mkwati anabwera panali nthawi yakuti anamwali akonze nyali zao? Ai, panalibe nthawi. Panali nthawi yambiri iye asanabwere. Fanizo limeneli likutiphunzitsa kuti pa kubweranso kwa Ambuye padzakhala popanda mwayi kapena mpata okonzekera.

Nanga ndi liti tiyenera kukonzekera? Buku Lopatulika limati "Taonani, tsopano ndiyo nyengo yabwino yolandiridwa, taonani, tsopano ndilo tsiku la cipulumutso" (2 Akorinto 6:2b). Ife sitidziwa kuti imfa idzafika liti. Koma pamene idzabwera, kudzakhala kobvuta kukonzekera kuti tikumane ndi Mulungu cifukwa tidzacedwa. Motero aliyense wa ife tiyenera kutsimikiza za cipulumutso cathu tsopano.

GAWO LACINAI:

Pali phunziro linanso lomwe fanizoli limatiphunzitsa ife. Anamwali opusa sanakhoze kupatsidwa mafuta kucokera kwa anamwali ocenjera. Munthu sangathe kubwereka cilungamo ca ciyanjano ndi Ambuye kucokera kwa wina aliyense. Nthawi zina tikafunsa munthu kuti, "kodi ndiwe Mkristu?" amayankha kuti, "Oh, inde. Makolo anga ndi Akristu. Cifukwa ca cimeneci inenso ndine Mkristu." Fanizo limeneli limatiphunzitsa ife kuti munthu aliyense ayenera kukonzekera motero kuti akumane ndi Ambuye Yesu. Palibenso wina wace amene angatikonzere. Ife sitingathe kubwereka kukonzekeraku kucokera kwa mwini wace.

MTSOGOLERI:



GAWO LACINAI:

Kodi cimene cimapangitsa munthu kuti akhale osasowa pamaso pa Mulungu ndi ciani? Mulungu akuti, "cifukwa moyo wace wa munthu sulingana ndi kucuruka kwa zinthu zace ali nazo" (Luka 12:15b). Munthu angakhale ndi zinthu zambiri koma pamaso pa Mulungu angakhale osowa. Munthu amene aika Mulungu poyamba ndiye amene ali wacuma pamaso pa Mulungu.

Mdziko lapansi muli anthu ambiri amene ali ndi cuma cosanena. Amagwiritsira nchito cuma cao pa ulemerero wa Mulungu. Amapereka cuma cambiri pofuna kuthandiza nchito ya Mulungu pa dziko lonse lapansi. Amathandiza anthu ambiri ndi zinthu zimene Mulungu anawapatsa. Palinso anthu ambiri amene alibe cuma cambiri. Koma naonso amacita zinthu zambiri pothandiza nchito ya Mulungu pa dziko lonse lapansi. Conco kusasowa kwa munthu sikumaonekera ndi zinthu zomwe ali nazo ai. Kumaonekera ndi malo amene Mulungu ali nao m'moyo wace. Kumaonekeranso ndi zomwe amacita ndi zinthu zace.

Tiyenera kugwiritsa nchito cuma cathu m'njira zimene zizakondweretsa Mulungu. Tikatero tidzazikundikira cuma kumwamba. Tidzakhala a cuma m'zinthu za Mulungu.

MTSOGOLERI:

Mau apamtima alero akuti, "Pakuti kumene kuli cuma cako, komwe udzakhala mtima wakonso" (Mateyu 6:21). Kodi mtima wanu uli kuti lero? Kodi uli pa zinthu za Mulungu? Kapena uli pa zinthu za dziko lapansi? Tiyeni tipemphere kuti Mulungu adzatipatsa nzeru kuti tifunefune zinthu za Mulungu koposa zinthu zina. Tipempheranso kuti Mulungu ationetse m'mene tingagwiritsire nchito cuma cathu pa nchito yace.

PEMPHERO:

MUTU 7

PHUNZIRO LA GAWO: MAFANIZO A YESU

PHUNZIRO LALERO: ANAMWALI KHUMI

MAU A MULUNGU: Mateyu 25:1-11

MAU APAMTIMA: **"Cifukwa cace khalani inunso okonzekeratu; cifukwa munthawi m'mene simunganizira, Mwana wa munthu adzadza."**

**Mateyu 24:44**

MTSOGOLERI:

Tiri kukumbutsidwa kaciwiri kuti Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri m'mafanizo. Mafanizo amenewa anathandiza anthu kuti akumbukire zoonadi za Mulungu. Yesu anali kuyandikira ku nthawi ya imfa yace ndi kuukanso. Mutu 24 m'buku la Mateyu, Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri za kubweranso kwace. Akuphunzira anafuna kudziwa kuti nthawi imeneyi idzakhala liti. Yesu anaphunzitsa kuti sicinali cofunikira kweni kweni kudziwa za nthawi yakubweranso kwace. Kudzakhala kodzidzimutsa ndipo palibe wina aliyense amene adziwa koma Mulungu yekha ndiye adziwa kuti lidzakhala liti (Werengani Mateyu 24:26). Cinthu cofunika ndi cakuti munthu aliyense akhale okonzekera kubweranso kwa Ambuye (Werengani Mateyu 24:44).

GAWO LOYAMBA:

Pofuna kuthandiza anthu kuti amvetsetse za kukhala okonzekera kubweranso kwa Ambuye Yesu Kristu, Yesu anawafotokozera fanizo. Tsegulani Buku Lopatulika lanu pa Mateyu 25:1-13.

Mu ndime izi Yesu anali kulankhula za kanthu kena komwe kanali kucitika kawiri kawiri m'midzi m'nthawi ya moyo wace. Timauzidwanso kuti cimacitikabe masiku ano m'dziko la Palestine kapena m'maiko momwe Yesu anayendamo. Panali anamwali omwe



anatenga nyali zao ndipo anaturuka kupita kukayembekezera kubwera kwace kwa mkwati. Asanu mwa anamwaliwo anali opusa cifukwa analephera kutenga mafuta a nyali zao.

Iwo anayembekezera kubwera kwace kwa mkwati kwa nthawi yaitali. Iye anabwera mocedwa. Patapita nthawi anamwali aja anagona tulo. Ndipo pakati pa usiku panamveka kupfuula, "Onani mkwati! turukani kukakomana naye" (Mateyu 25:6b).

Anamwali onse ananka nayamba kukonza nyali zao. Opusa aja anati kwa anzao anzeruwo, "Tipatseniko ena a mafuta anu; cifukwa nyali zathu zirikuzima" (Mateyu 25:8). Anamwali ocenjera aja anakana cifukwa iwo anali ndi mafuta okwanira nyali zao zokha. Anamwali opusa anayesa kupeza mafuta a nyali zao. Pamene iwo anali kufuna funa mafuta, mkwati anafika. Ndipo onse amene anali okonzekera kubwera kwace analowa naye m'nyumba ya mphwando. Ndipo citseko cinatsekedwa. Panalibe wina aliyense analoledwa kulowa m'nyumbamo. Pamene anamwali asanu opusa aja anafika, sanakhoze kulowamo. Citseko cinatsekedwa ndipo iwo sanakhale nao pa phwando.

GAWO LACIWIRI:

Mau a Mulungu amatiphunzitsa kuti Yesu Kristu adzabweranso. Amatiphunzitsanso kuti palibe munthu adziwa tsiku lace kapena nthawi imene adzabweranso. "Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku" (1 Atesalonika 5:2). Ndikofunikira kuti munthu aliyense adzakumane ndi Ambuye pamene adzabwera.

Kodi munthu angakonzekere bwanji kubwera kwace kwa Yesu Kristu? Poyamba, munthu ayenera kulapa macimo ace ndi kulandira Yesu monga Mpulumutsi wace. Yesu anafa kuti macimo a anthu akhululukidwe kupyolera mwa cikhulupiriro ca mwa Iye (Werengani Aroma 3:25a.)

Munthu atakhala Mkristu amayenera kukhala m'njira yokondweretsa Mulungu. Iye amayenera kufuna cifuniro ca Mulungu pa moyo